# CHIMWASONGWE PRIMARY SCHOOL

## 2024 ZONAL MOCK EXAMINATION

## CHICHEWA (100 MARKS)

Time allowed: 2¼ hrs

Name of Candidate: ______________________________________________

Name of School: ________________________________________________

**GAWO A** (Malikisi 30)

Langizo: Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'musiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena wa kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 koma asabzole 150

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu: **MAPHUNZIRO**
   Mwa zina tsatani izi polemba

   **Ndime yoyamba**
   - Komwe maphunziro amapezeka
   - Ena mwa anthu ndi mabungwe omwe amathandiza pa nkhani ya maphunziro

   **Ndime yachiwiri**
   - Zovuta zomwe zimapangitsa kuti maphunziro asayendebwino
   - Njira zoyenerera kutsatira kuti maphunziro aziyenda bwino

   **Ndime yachitatu**
   - Kufunika kwa maphunziro

**KAPENA**

2. Lembani kalata kwa m'bale wanu yemwe amakhala kutali ndi inu yomufotokozera chitukuko chomwe chachitika kumudzi kwanu. Mwa zina tsatani izi polemba

   **Ndime yoyamba**
   - Fotokozani chitukuko chachitikacho
   - Tsiku, mwezi ndi chaka chomwe chitukukocho chidayambira

   **Ndime yachiwiri**
   - Momwe chitukuko chidayambira
   - Fotokozani zomwe mudachita pachitukukocho
   - Fotokozani momwe chitukukocho chakulira mudzi mwanu

   **Ndime yachitatu**
   - Zomwe mukuchita kuti chitukukocho chipitilire
   - Momwe mungalimbikitsire m'bale wanuyo kuti abwere kumudziko

**GAWO B** (MALIKISI 20)

**KUMVETSA NKHANI**

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawa

Kudali chakumadzulo kwa tsiku Lamulungu pomwe mnyamata wina dzina lake Katondo ankaperekeza wokondedwa wake, Namanyada Kumalo wokwerera basi a Mferekwanu. Panthawiyi n'kuti misonzi yothamanga ndi yotentha ngati madzi ikutsikira m'masaya mwa mnyamatayo. Kumeneku kudali kulira polingalira kuti wachikondi wakeyo amachoka kupita kukagwira ntchito ku Zimbabwe.

Basi yomwe adakwera Namanyada isadafike Katondo ndi wokondedwa wakeyo adali kucheza. Pamenepa Katondo adamuuza wokondedwa wakeyo kuti Chikondi chake sichidzasintha ngakhale atakumana ndi mikwingwirima yotani. Adamuuzanso kuti ndibwino kuti njoleyo isunge khosi kuti nkanda woyera idzavale mtsogolo. Adamukumbutsanso kuti kunja kuno kwaopsa choncho n'kofunika kusamala.

Ngakhale mnyamatayo adafotokoza zonsezi, kudali kungotaya nthawi chifukwa kwa njoleyo zinkangotulukira mbali ina ya khutu. Zoona zenizeni zidali zakuti Namanyada sankamukonda mnyamatayo chifukwa adali mphemvu mdyera kunthiko, kwakwatuke wachabechabe.

Atayamba ntchito ija, mtima wake udaloza kwa njonda ina yomwe idali yokhupuka. Sipadatenge nthawi yayitali, Namanyada adamutsiya Katondo uja ndipo adakwatiwa ndi njonda ija ngakhale idali ndi mkazi wina kale. Makolo a Namanyada adayetsetsa kumuletsa koma poti mwana akalirira nyanga ya nsatsi msemere imufotere yekha adangomusiya.

Patapita nthawi Namanyada adapezeka ali ndi pathupi. Atapita ku sikelo ya amayi oyembekezera kuchipatala adamuyeza ndipo adamupeza kuti ali ndi kachirombo koyambitsa Edzi ka HIV. Pamenepo adakumbukira malangizo a bwenzi lake Katondo. Koma poti madzi akatayika saoleka, iye adalira ndi kunong'oneza bondo.

**Mafunso**

(a) Kodi pakati pa Katondo ndi Namanyada padali ubale wanji?

____________________________________________________ (Malikisi 1) (b)

Kodi malo amene adakwerera basi Namanyada ankatchedwa chiyani?

____________________________________________________ (Malikisi 1)

(c) N'chifukwa chiyani misonzi ya Katondo inkatsikira m'masaya?

__________________________________________________________

____________________________________________________ (Malikisi 2) (d)

Nchifukwa chiyani Namanyada adapita ku Zimbabwe?

____________________________________________________ (Malikisi 1) (e)

Kodi Namanyada ankafuna mwamuna wotani?

____________________________________________________ (Malikisi 1)

(f) N'chifukwa chiyani makolo a Namanyada adamuletsa kukwatiwa ndi njonda ija?

__________________________________________________________

____________________________________________________ (Malikisi 2)

(g) Perekani zining'a kuchokera m'nkhaniyi zomwe matanthauzo ake ndi awa:
i. Mkazi wokongola ______________________________________________ (Malikisi 1) ii. Mavuto ____________________________________________________ (Malikisi 1)

(h) Perekani tanthauzo la mkuluwiko uwu kuchokera m'nkhaniyi; "isunge khosi kuti mkanda woyera idzabvale"

______________________________________________________________________________

____________________________________________________________________ (Malikisi 2)

(i) Fotokozani chifukwa chimene Namanyada adanong'onezera bondo?

______________________________________________________________________________

____________________________________________________________________ (Malikisi 2)

(j) Kodi matenda a Edzi amaopsa bwanji?
____________________________________________________________________ (Malikisi 1) (k) Pezani mawu ofanana m'matanthauzo ndi otsatirawa kuchokera m'nkhaniyi?

i. Pakati ____________________________________________________ (Malikisi 1)

ii. Yokhupuka ______________________________________________ (Malikisi1)

iii. Polingalira ______________________________________________ (Malikisi 1)

iv. Perekani mutu wa nkhaniyi.
____________________________________________________________________ (Malikisi 2)

**GAWO C:**
Yankhani mafunso onse awiri m'gawoli
4. Werengani kankhanika mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.

A Chiutula: Chete! Chete! Ulemu kwa mfumu, ulemu kwa anzanga, ulemu kwa amayi ndi abambo, moni nonse.

A Chiutula: Zikomo chifukwa cha kubwera kwanu mwaunyinji, ndikudziwa mutamva uthenga dzulo usiku munagona khutu liri kukhomo. Mfumu yathu ndiyo ili ndi mawu. Zikomo Mfumu. **Mafunso**

(a) i. Kodi a Chiutula ali ndi udindo wanji m'kankhanika?

____________________________________________________________________ (Malikisi 1)

ii. Perekani tanthauzo la mawu oti, "Kugona khutu liri kukhomo"
____________________________________________________________________ (Malikisi 1)

(b) Lembani kuipa kumodzi kogwiritsa ntchito kalata ngati njira imodzi yotumizira uthenga?

____________________________________________________________________ (Malikisi 1)

(c) Kodi mnyamata wachimalawi akamayankhula ndi munthu wankulu amayenera kutani?

____________________________________________________________________

____________________________________________________________________ (Malikisi 2)

(d) Kodi ndi malonje anji munkhaniyi?

________________________________________ (Malikisi 1)

5. **Kupanga ziganizo**

Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

(a) choncho ________________________________ (Malikisi 1)

(b) zakuda ________________________________ (Malikisi 1)

(c) mkoko ________________________________(Malikisi 1)

(d) mwamphamvu ________________________________ (Malikisi 1)

(e) bii ________________________________ (Malikisi 1)

**Gawo D. (Malikisi 40)**

**Mafunso 6 mpaka 10.** Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kundi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

6. Mvula imachokera kunyanja
   A. Dzina
   B. Mfotokozi
   C. Mneni
   D. Muonjezi
7. Agogo apeza dzungu pakati pa munda
   A. Mlumikizi
   B. Mperekezi
   C. Mlowammalo
   D. Dzina
8. Ana anali balala kuthawa gulewankulu
   A. Mvekero
   B. Mlumikizi
   C. Mneni
   D. Muonjezi
9. Ng'ombe zamphamvu zimakoka ngolo
   A. Mfotokozi
   B. Mvekero
   C. Muonjezi
   D. Mneni
10. Pamene Nasimero amatunga madzi, Nakonyani amaphika nsima
   A. Dzina
   B. Mneni
   C. Mfotokozi
   D. Muonjezi

**Mafunso 11 mpaka 13.** Sankhani gulu la mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi

11. Kalata yapatsidwa lero
   A. Ka-, Ti-.
   B. I-, Zi –.
   C. Chi-, Zi –.
   D. Li-, Ma –.
12. Matiyasi amakonda kuwerenga
   A. Ku-, Pa-, Mu –.
   B. I-, Zi –.
   C. Chi-, Zi –.
   D. Ku – nditsinde la mneni.
13. Anawa amakonda malalanje
   A. Li-, Ma –.
   B. Mu-, Mi –.
   C. I -, Zi –.
   D. U -, Ma –.

**Mafunso 14 mpaka 18**. Sankhani mitundu ya misintho ya aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi

14. Mwanayu wandimenyetsa
   A. Wochititsitsa
   B. Wochitirana C. Wochititsa
   D. Wochitidwa
15. Akuba awululana
   A. Wochititsa
   B. Wochitirana C. Wotsutsa
   D. Wochitidwa
16. Ife atimangira nyumba
   A. Wotsutsa
   B. Wochitidwa
   C. Wochitirana
   D. Wom'chitira
17. Ndani wamasula mbuzi yanga pamtengo?
   A. Wom'chitira
   B. Wochitidwa
   C. Wochitirana
   D. Wotsutsa
18. Amalume akhapidwa ku mowa
   A. Wochitirana

B. Wochitidwa
C. Wochititsa
D. Wochititsitsa

**Mafunso 19 mpaka 22.** Sankhani matanthauzo a ndagi zotsatirazi

19. Nkhuku yayikira dzira paminga
    A. Njoka
    B. Chisoso
    C. Chisoni
    D. Lilime
20. Nkhwangwa yanga mtema patali
    A. Diso
    B. Dzina
    C. Khadabo
    D. Khutu
21. Kungatalike lero lomwe n'kafika
    A. Ndege
    B. Mitambo
    C. Namzikambe
    D. Maganizo
22. Khasu la akazi kwina kolimira kwina kosalazira
    A. Chipande
    B. Kasememasema
    C. Mano
    D. Sefa

**Mafunso 23 mpaka 26.** Sankhani mitundu ya afotokozi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

23. Ndikupatsani mbuzi <u>zitatu</u> zokha
    A. Waumwini
    B. Wamawerengo
    C. Wamgwirizano
    D. Wochuluka
24. Walumidwa ndi galu <u>wachiwewe</u>
    A. Wamakhalidwe
    B. Wamgwirizano
    C. Waumwini
    D. Wamaonekedwe
25. Chimwana <u>chimene</u> chikuliralirachi n'chayani?
    A. Wamgwirizano
    B. Waummwini
    C. Wofunsa
    D. Wamakhalidwe
26. Wavala buluku <u>loyera</u>
    A. Waumwini
    B. Wamaonekedwe
    C. Wamakhalidwe
    D. Wamawerengo

**Mafunso 27 mpaka 31**. Sankhani ntchito za mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

27. <u>Mafiyo,</u> bwera uzadye
    A. Mwininkhani
    B. Mtsirizitsi wa mneni
    C. Loitanira
    D. Pamtherankhani
28. Tigula <u>galimoto</u> chaka chino
    A. Mwininkhani
    B. Lapadera
    C. Mwinichinthu
    D. Pamtherankhani
29. Wakwatira Nabetha, <u>njole</u> yapatsidyapa
    A. Lapadera
    B. Pamthera nkhani
    C. Loitanira
    D. Mwininkhani
30. Mpatseni chakudya mwanayo, <u>amayi</u>
    A. Pamtherankhani
    B. Loitanira
    C. Mwininkhani
    D. Mwinichinthu
31. <u>Jekapu</u> wagula njinga
    A. Mwininkhani
    B. Loitanira
    C. Mwinichinthu
    D. Pamtherankhani

**Mafunso 32 mpaka 36**. Sankhani mitundu ya nthambi za ziganizo zosaima pazokha zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

32. Muuzeni <u>kuti aphike nsima ya agogo</u>
    A. Ya dzina
    B. Ya mfotokozi
    C. Ya muonjezi
    D. Yoyima payokha
33. Iwo adafika <u>tonse titagona</u>
    A. Ya mfotokozi
    B. Yoyima payokha
    C. Ya dzina
    D. Ya muonjezi
34. Abwera <u>pokhapokha mutamutumizira uthenga</u>

A. Yoyima payokha
B. Ya muonjezi
C. Ya mfotokozi
D. Ya dzina

35. Chaipa waba nkhuku <u>yomwe adagula agogo</u>
A. Ya muonjezi
B. Ya mfotokozi
C. Ya dzina
D. Yoyima payokha

36. Amvana <u>zoti atichite chipongwe</u>
A. Ya mfotokozi
B. Yoyima payokha
C. Ya dzina
D. Ya muonjezi

**Mafunso 37 mpaka 40**. Sankhani mitundu ya kanenedwe ka aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

37. Sikunache <u>musadzuke</u>
A. Kofotokoza
B. Kolamula
C. Kachifuniro
D. Kacholinga

38. Tabwera kuti <u>titenge</u> njinga
A. Ka cholinga
B. Kofotokoza
C. Kolamula
D. Kachifuniro

39. Ife amnzanu <u>tabwera</u> kale
A. Kolamula
B. Kacholinga
C. Kofotokoza
D. Kachifuniro

40. Mulungu <u>akudalitseni</u>
A. Kofotokoza
B. Kachifuniro
C. Kacholinga
D. Kolamula

**Mafunso 41 mpaka 46**. Sankhani matanthauzo a zining'a zotsatirazi.

41. Kalowam'malaya
A. Nsabwe
B. Njala
C. Nsalu
D. Singano

42. Sisitira bondo
A. Nyamakazi
B. Langiza
C. Zengereza
D. Binya

43. Chulu cha ndiwo
A. Wamantha
B. Wankhuli
C. Wopusa
D. Womana

44. Loza ndege ndi chala
A. Yaluka
B. Nyada
C. Temberera
D. Tukwana

45. Kamwendo m'njira
A. Wolumula
B. Wamantha
C. Woyendayenda
D. Wamtali

46. Samva mkunkhu
A. Wosamva
B. Wosauka
C. Wolemera
D. Wopilira

**MAFUNSO ATHERA APA**